Chichewa التشيشيوا

# 3 MITUNDU YA TAUHEED

Kumupatula Allah (olemekezeka) muzinthu zimene wapatulika nazo, kumbali ya umbuye,umulungu ndi maina komanso mbiri zake.

NDIPO MITUNDU YAKE ILIPO ITATU:

### Tauheed ya umbuye (al-rububiyyah)

Kumeneko ndiko kumupatula Allah pa zintchito zake, kapena kumupatula Allah pa kulenga, umwini pa chilichonse ndi kuyendetsa zinthu.

### Tauheed ya umulungu (al-uluhiyyah)

Uku ndiko kumupatula Allah pompembedza, kapena pa zintchito za akapolo.

### Tauheed ya maina komanso mbiri za Allah (al-Asmâu wa swifat)

Uku ndiko kumupatula Allah pa maina omwe wazitchulira yekha kapena mbiri zomwe wazifotokoza yekha mu buku lake la Quran, kapena kudzera pa lilime la Mtumiki wake mtendere ndi madalitso zipite kwa iye.Kumupatulaku kwagona potsindika zomwe iye mwini watsindika, ndikuzikana/kuzitsutsa zomwe mwini wake azitsutsa, mopanda kusintha kapena kuchotsa mbiri zonse kapena zina mu mbiri za Allah,mopandanso kunena kuti mbiri zakezo zili bwanji(mwachitsanzo kunena kuti:ngati wakhala wakhala motani?), komanso mopanda kufanizila ndi mbiri za zolengedwa zake.

## Ndondomeko(mndandanda) wa chipembedzo uli mmagulu atatu:

### AL ISLAM (CHISILAMU)

Kumeneko ndi kuzipeleka mwa Allah pomupatula,ndi kugonjera mwa iye pomumvera, komanso kuzitalikitsa ku shiriki ndi anthu opanga za shiriki wo.

**NSICHI ZA CHISILAMU: 5**

1-Ma shahada awiri.
2-Kuimika swala.
3-Kupeleka chaulele(zakah).
4-kusala kudya(swaum) mmwezi wa Ramadhani.
5-Kukapanga Hajj ku nyumba yolemekezeka,kwa yemwe ali ndi kuthekela kokafika kunyumbayi.

### AL IMAN (CHIKHULUPILIRO)

Uku ndiye kuyankhula ndi lilime ndi Kutsimikiza ndi mtima,kugwira ntchito kudzera mu ziwalo. Chikhulupiliro chimaonjezereka komanso chimapunguka.

**NSICHI ZA CHIKHULUPILIRO: 6**

1-Kukhulupilila mwa Allah.
2-Mwa Angelo ake.
3-Mabuku ake.
4-Atumiki ake.
5-Za tsiku lomaliza.
6-Ndi kukhulupilila za chikhozero chabwino ndi choipa kuti zonsezo zimachokera kwa Allah.

### AL IHSAN(UBWINO)

Kumupembedza Allah ngati ukumuona, ngati zili zakuti siukumuona ndiye udzindikire kuti iyeyo akukuona.

**Nsichi imodzi pansi pake pali ndondomeko/ ma sitepe awiri:**

1-mapemphero akuona: Umpembedze Allah ngati ukumuona.
2-mapemphero akuyang'anilidwa: Ngati siukumuona zindikira kuti iyeyo akukuona.

## 4 MAGULU AZINTHU ZOLETSEDWA (HARAM)

### MACHIMO ANG'ONO ANG'ONO

Awa ndi machimo omwe sanafike mulingo wa machimo akulu akulu. Machimo akulu akuluamachotsedwa (kufufutidwa)popempha chikhululuko ndipo machimo ang'ono ang'ono amasanduka kukhala akulu akulu ngati munthu akupitilira kuwapanga panga, Mtumiki madalitso ndi mtendere zipite kwa iye adati: "Atalikileni machimo ooneka monyozeka (ang'ono ang'ono) chifukwa machimo amenewo amasonkhana mwa munthu kufikila kuti amadzamuononga munthuyo".

### MACHIMO AKULU AKULU

Chilichonse chimene chalumikizidwa ndi chilango chopatulika pa tchimo limenelo. Machimo amenewa ndi monga: Ufiti,Kunyoza makolo awiri, katapila,Chigololo,kugonana amuna kapena akazi okha okha, bodza, kumwa mowa, kuba, miseche,kupha munthu popanda chifukwa chovomerezeka ndi sharia, komanso kudya chuma cha ana a masiye.

### Shiriki yaing'ono

Mtundu uwu wa shiriki siumtulutsa munthu mu chipembedzo,koma kuti ndi tchimo lalikulu m'machimo omwe ali akulu akulu.Mwachitsanzo ngati kuyankhula kuti : izi ndi zomwe wafuna Allah ndi iweyo (maa Shaa Allah wa shiita), kulumbila mosakhala mwa Allah, kuzionetsera kwakung'ono (riyah yaing'ono)kupachika zithumwa,kudziwa mwayi kapena tsoka kuchokera mu mbalame, ndi zinthu zina zochuluka zimene munthu angazipange kukhala zida zozitetezera kapena kuti zimenezo zitha kumuteteza ku ufiti.

### Shiriki yaikulu

Iyi imamutulutsa munthu mu chipembedzo,ndipo samakhululukidwa ngati wamwalira ali pa shiriki yo. Wa shiriki yaikulu amamuikila Allah timilungu tina ndikumatipembedza kapena kutipempha ngati mmene amamupemphera Allah, kapena amalakalaka kena kake kuchokera ku timilungu timeneto kapena kutikonda ngati m'mene angamukondele Allah, kapena amakhala akutipangila mtundu wina wake wa mapemphero .